Kodi phindu loneneza za chinyengo ndi lotani?

Ngati zomwe mwanena zithandiza kugwira anthu ozembetsa msonkho ndipo a MRA atolera msonkho pa katundu wozembetsedwayo mudzalandira chiona maso. Mungathe kupeza mphoto zochuluka mpaka kufika pa **MK500, 000.**

Mukapereka umboni wanu ku nambala ya **847** ma ofisala amafufuza mwa changu za nkhaniyo. Izi zimachitika nthawi ina iriyonse ndiponso tsiku lina lirilonse ndipo nthawi ina iliyonse.

Pa chifukwa ichi, tikukupemphani kuti muneneze za chinyengo zonse zomwe inu mukuzidziwa maka pozemba msokho kapena katangale kuti MRA itolere ndalama zothandizira kutukula dziko lathu la Malawi.

Ngati mufuna kudziwa zambiri muntha kuyimba Nambala izi: 0888952571, 0888958220 kapena 01822588.

Produced by Corporate Affairs Division - MRA

Malawi Revenue Authority
Msonkho House
Independence Drive
Private Bag 247
Blantyre

Tel: +265 - 1 822 588
Fax: +265 - 1 822 302
E-mail: mrahq@mra.mw
Web: www.mra.mw

Develop Malawi, Pay Taxes

Kumvesetsa Za...

MRA TIP-OFFS ANONYMOUS SERVICE

KUNENEZA ANTHU OZEMBETSA MSONKHO

Mungathe kupeza mphoto zochuluka mpaka kufika pa MK500, 000 ngati papezeka umboni wokwanira.

Kodi Tip Offs Anonymous Service ndi chani?

Pofuna kuthana ndi mchitidwe wa katangale, ziphuphu komanso kuzembetsa katundu posafuna kulipira msonkho, a Malawi Revenue Authority (MRA) anakhazikitsa njira ya chinsinsi yomwe inu mungagwiritse ntchito kuneneza anthu amene mukuwadziwa kapena kuganizira kuti akuchita chinyengo pa nkhani ya msonkho.

Njirayi ndi yaulere yomwe ingakuthandizeni kuneneza zachinyengo zomwe zimachikita malo ogwirira ntchito komaso ochitila bizinesi.

Kwa omwe ali ndi umboni woti msonkho ukuzembetsedwa kapena katundu akulowa ndi kutuluka mdziko muno mwa chinyengo, angathe kuyimba lamya mwaulere pa nambala ya **847** kwa onse ogwiritsa ntchito foni za **Airtel** ndi **TNM** ndipo **80000847** kwa onse ogwiritsa ntchito foni za **MTL.**

Mungathe kuyankhula mchiyankhulo cha Chichewa kapena mchingerezi malinga ndi kufuna kwanu.

Njirayi ndi ya chinsinsi.

Mungathenso kuneneza za chinyengo polemba kalata ndikutumiza ku keyala iyi mwaulere:

The Call Centre,
P.O. BOX 1726, Blantyre.

Kuyambira Lolemba mpaka lachisanu nthawi za 7:30 mmawa mpaka 5:30 madzulo (kuphatikiza ndi masiku atchuthi), muli ndi mwayi wolankhula ndi kuthandizidwa moyenera ndi anthu omwe amalandira maripoti anu. Ndipo loweruka mungathe kulankhulana ndi ma ofisala kuyambira 8:00 mmawa mpaka 12:00pm.

Pogwiritsa ntchito njirayi muyenera kupereka tsiku lomwe za chinyengozo zikuchitikira olo zinachitikira, nthawi, dera, anthu omwe anakhuzidwa ngati mukuwadziwa, ndiponso kuchuluka kwa katundu yemwe akuzembetsedwa kapena anazembetsedwa.

Mungathe kuyankhula mchiyankhulo cha Chichewa kapena mchingerezi malinga ndi kufuna kwanu. Mudzafunsidwa kupereka nambala zisanu monga 21455 kapena 52212, mwa chitsanzo chifukwa simukuyenera kupereka dzina lanu poti njirayi ndi ya chinsinsi. Nambala yoimira dzina lanuli simuyenera kuitaya.

Izi zili choncho chifukwa ngati umboni wanu wapangitsa kuti titolere msonkho, nambala yanu ya chisinsi ija timasindikiza munyuzi pepala kuti mulandire mphoto yanu.